**Funso**:

Kodi afiti aja ali ndi mphamvu yopeleka nthenda kwa munthu? Ngati ndi ayi, zimatheka bwanji kut iwowo azipanga matsenga awowo kulodza munthu? Ngati eya, mphamvuzo amazitenga kuti?

**Yankho**:

Kutamandidwa konse ndi kwa Allāh!

Choyamba, Allāh akuyankhulapo zokhudza afiti motere:[1]

وَمَا هُم بِضَآرِّينَ بِهِ مِنْ أَحَدٍ إِلَّا بِإِذْنِ اللَّهِ.

*Koma iwowo savulaza aliyense kudzera mu iwo (ufitiwo) kupatulapo mu chilolezo cha Allāh.*

Ibn Kathīr ndi Abī Hātim adafotokoza kuti:[2]

قَالَ سُفْيَانُ الثَّوْرِيُّ: إلا بِقَضَاءِ اللَّهِ، وقال الحسن البصري: مَنْ شَاءَ اللَّهُ سَلَّطَهُمْ عَلَيْهِ وَمَنْ لَمْ يَشَأِ اللَّهُ لَمْ يُسَلِّطْ، وَلا يَسْتَطِيعُونَ ضَرَّ أَحَدٍ إلا بِإِذْنِ اللَّهِ.

*Adayankhula Sufyān Ath-Thawrī: "Kupatulapo mu chilamulo cha Allāh." Ndipo Al-Hasan Al-Baswrī adati: "Yemwe Allāh wamufuna (kuti ufitiwo umugwere), amawapangitsa iwowo (afitiwo) kumuchita zomwe akonzazo. Ndipo yemwe Allāh sadamufuna (kuti usamugwere), iwowo sakwanitsa. Ndipo afiti sabweretsa vuto pa aliyense kupatulapo kudzera mu chilolezo cha Allāh."*

Ibn Is-hāq adati:[3]

أَيْ بِتَخْلِيَةِ اللَّهِ بَيْنَهُ وَبَيْنَ مَا أَرَادَ.

*Kutanthauza kuti: "Kusiidwa kumene Allāh amachita pakati pa kapoloyo ndi zomwe Allāh wafuna."*

Mu gawo limene adayankhula Ibn Is-hāq tipezamo zinthu zitatu:[4]

---

[1] Sūrah Al-Baqarah 2:102
[2] Tafsīr Ibn Kathīr, Vol. 1, tsamba 364; Tafsīr Ibn Abī Hatim, Vol. 1, tsamba 193, 194
[3] Tafsīr Ibn Abī Hatim, Vol. 1, tsamba 193
[4] Al-Kifāyah fi At-Tafsīr bil Ma'thūr, Vol. 3, tsamba 69

Pa chifukwa ichi, mfiti aliyense alibe mphamvu yobweretsa vuto kwa wina aliyense. Ngati zomwe iyeyo wakonza zamuvulaza wina wake, zimenezo ndi zomwe Allāh waloleza kudzera mu uzindikiri Wake komanso chikonzero Chake. Ndipo yemwe ufitiwo sudamufikire, ameneyo watetezedwa ndi Allāh kudzera mu chikonzero Chake.

Choncho, ufiti suvulaza aliyense kupatulapo yemwe akuuchitayo. Chifukwa ena omwe akupangiridwa ufitiwo amakhala kuti akudutsa mu zimene Allāh wawakonzera. Iwowo akhonza kutetezedwa ndi Allāh, kapena Allāh akhonza kuwasiya kuti uwagwere ndi cholinga choti apirire ndi kulandira malipiro ochuluka kuchokera kwa Allāh ngati ali okhulupirira.

Adayankhula Al-Hasan Al-Baswrī kuti:[5]

لَا يَضُرُّ هَذَا السِّحْرُ إِلا مَنْ دَخَلَ فِيهِ.

*Suvulaza ufiti umenewu kupatulapo amene waulowa (amene amauchita).*

[5] Tafsīr Ibn Abī Hatim, Vol. 1, tsamba 193